## UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

**NYENGO MSABATAYI**


**KUYAMBIRA PA 26 AUGUST MPAKA 1 SEPTEMBER, 2024**


### NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Kuchokera mawa Lolemba pa 26 August 2024 mpaka lachinayi pa 29 August 2024, tiyembekezere nyengo ya mphepo, yamitambo yapatali patali komanso yotentha. Izi ndi kamba ka mpweya ofunda ochokera kumvuma. Koma pomafika madzulo a lachinayi kudzakhala kutayamba nyengo ya Chiperoni yomwe ndi yamphepo, yozizila komanso yamvula yamawawa ndi chifunga. Izi ndi chifukwa cha mphepo zozizila komanso zachinyotho zochokera kumwera cha kumvuma. ***Mphepo ya mvuma idziomba pa Nyanja zathu nthawi zina koma kuyambira lachinayi madzulo mphepo ya Mwera ikuyembekezereka kuomba mwamphanvu***.

### NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Kunazizira kwambiri m'sabatayi makamaka nthawi ya ku m'mawa. Ndipo ma digiri anatsika kufika pa mlingo wa **7.5 Celcius** ku bwalo la ndenge ku KIA pa 19 August 2024 komanso ku Dedza pa 24 August 2024. Poyerekeza ndi zaka zam'mbuyomu madigiri anatsika kwambiri ku Mzimba ndi mlingo wa madigiri -**5.2 Celcius** pa **19 August, 2024. Ngakhale kunali nyengo yozizira kum'mawa, masana kunali kotentha m'madera ambiri ndipo ku Chileka mulingo wakatenthedwe unakwera ndi madigiri +2.4 Celcius pa 23 August 2024.**




**Chithunzi -chakumanzere: Mlingo wakazizilidwe. Chithunzi -chakumanja: Mlingo wakatenthedwe poyerekeza ndi milingo yokhazikika ya mwezi wa August (1991-2020).**

### MALANGIZO M'SABATALI

- Asodzi ndi ena ogwiritsa ntchito nyanja akhale osamala pomwe mphepo ya Mwera ikuomba.
- Kukakhala chifunga tikhale osamala panseu poyendetsa magalimoto ndi njinga zamoto.
- Tidzivala zovala mokwanira komanso tionetsetse kuti ana ndi okalamba akutetezedwa kuchisanu.
- Tipewe kuotha kapena kugwiritsa ntchito mbaula mawindo ndi zitseko zili zotseka.

***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 25 August, 2024**